



PHALOMBE DISTRICT EXAMINATION BOARD

2026 STD 8 MOCK EXAMINATION

CHICHEWA

(Malikisi 100)

Subject Number: P025

Time allowed: 2 $\frac{1}{4}$ hours

Time : 1:00pm – 3:15 pm

Date _____

Dzina lanu: _____

Dzina la Sukulu yanu: _____

Malangizo:

1. Onetsetsani kuti pepalali lili ndi masamba asanu ndi awiri.
2. Pepalali lili ndi magawo anayi; **A, B, C** ndi **D**. Sankhani funso limodzi lokha mu gawo A. Yankhani mafunso onse mumagawo ena otsalawo (**B, C** ndi **D**).
3. Mutebulo lomwe lili kumanja kwanu patsamba lino, chongani mutimabokosi tomwe mwapatsidwa mogwirizana ndi mafunso omwe mwayankha.
4. **CHENJEZO**
 - Onetsetsani kuti mwalemba dzina lanu, nambala yanu ya mayeso ndi dzina la sukulu yanu pa mipata yomwe mwapatsidwa.
 - Perekani pepala lanu kwa oyang'anira mayeso nthawi yolembera mayesowo ikatha.

Funso	Chongani ngati mwayankha	Muno musalembemo	
1			
2			
3			
4			
5			
6-10			
11-15			
16-20			
21-25			
26-30			
31-35			
36-40			
41 - 45			



GAWO A (MALIKISI 30)

Langizo: yankhani funso limodzi lokha mwa mafunso awiri ali m'musiwa. Sankhani chimangirizo kapena kalata. Mawu a chimangirizo chanu kapena kalata yanu asachepere **100** koma asabzole **150**.

1. CHIMANGIRIZO

Lembani chimangirizo pa mutu uwu: **"MVULA YA MPHAMVU"**

Mwa zina tsatani izi polemba:

Ndime yoyamba

- Tsiku lomwe mvula ya mphanvu idayamba
- Idayamba nthawi yanji?
- Idagwa masiku angati?

Ndime yachiwiri

- Madera omwe adakhudzidwa ndi mvulayo
- Mavuto omwe adabwera m'dera lanu chifukwa cha mvulayi

Ndime yachitatu

- Chithandizo chomwe anthu okhuzidwa ndi mvulayi adalandila

KAPENA

2. Lembani kalata kwa mzanu wa sukulu ina, yomuchenjeza kuti akapitiriza ndi makhalidwe oyipa omwe akuchita atha kuzalephera mayeso a boma akubwerawa.

Mwa zina tsatani izi polemba :

Ndime yoyamba

- Cholinga cha kalata
- Makhalidwe oipa omwe mnzanuyo akuchita
- Adayamba liti makhalidwe oiyipawo?

Ndime yachiwiri

- Amnzake omwe amacheza nawo amakhalidwe oyipawo.
- Zotsatira zomwe zadza kamba ka makhalidwe oyipawo

Ndime yachitatu

- Zomwe mnzanuyo angamachite kuti adzakhoze mayeso aboma

Learner's name :. _____

Examination number:._____

This image shows a single sheet of white paper with horizontal ruling lines. The lines are evenly spaced and run across the width of the page. There are no margins, text, or other markings on the paper.

GAWO B (MALIKISI 20)**KUMVETSA NKHANI**

3. Werengani nkhani yotsatirayi mosamala kwambiri kenaka muyankhe mafunso otsatirawa pa mizere ili pansi pa funso lililonse.

Chitamenyetsedwa chitsekochi idalowa njonda yamalamulo ovuta. Simunamvekenso phokoso mkalasimo, ndipo ophunzirawo adangoti zyoli. Ankadziwiratu kuti mphunzitsi wawo che Mphaka samaonetsa chitsakano pankhani zoduka mutu. “Mwalephera bwanji chonchi ntchito yanga?” adakalipa che mphaka. Umu nkuti akumasula lamba wa buluku lake. Ophunzirawo adangoti maso yuu pa iye ndipo ena adaganiza kuti kudali kuyamba kwa ziwala m’maso kwa munthu wa nzeruyo.

“Amene walakwa zisanu alandila malamba asanu ndipo yemwe wakhoza zonse anyadire mizimu yakwao. Ine kung’amba kukamwa konse kuja ndangozithira tsabola m’maso? Chibwana!” Posakhalitsa mudamveka phokoso lakukwapulidwa mkalasi muja.

Asanamalize kulanga ophunzira ozizira bongowo, padamveka kugogoda pachitseko. Adatuluka mphuzitsiyo, “ukuchokera kuti nthawi ino? Makope ali kuti? Muli chiyani nthumbamo?” sikadayankhe kamwana kadachedwako, botolo la thobwa lili m’manja. Kenako kanangotulusa botolo lina “koma zooni iwe ungaiwale kutenga makope nkukumbukira kutenga thobwa ndi chimanga chokazinga? Bwererani baba mukapitirize kumwa thobwa nkumwera chimanga chanucho.” Kamwanako kanangotembenuka nkuona nsana wanjira. Atabwerera mkalasi che Mphaka, adagwidwa ndi mantha nsungwana yemwe adamaliza kumukwapula adali lamba pansi.

“Melifa Melifa! Adaitana mphunzitsi uja, “tadzuka” Melifa sadayankhe. Maso ake adali chitsekere. “kalanga ine! Melifa wacomoka eti” che Mphaka adatero thukuta lili kamukamu.

Tsopano yankhani mafunso otsatirawa

- a. Kodi che Mphaka ndi yani? (Malikisi 1)

- b. N’chifukwa chiyani ophunzira adangozyolika mkalasi muja? (Malikisi 2)

- c. Fotokozani chifukwa chimene che Mphaka adawakalipila ana. (Malikisi 2)

- d. Kodi che Mphaka amatanthauzani ponena kuti “amene walakwa alandila malamba asanu?”

_____ (Malikisi 1)
- e. Perekani makhalidwe awiri a che Mphaka (Malikisi 2)
 - i. _____
 - ii. _____
- f. Ndani adagogoda chitseko pomwe che Mphaka amawalanga ophunzira mkalasi muja? (malikisi 1)

- g. Perekani mivekero iwiri munkhaniyi
 - I. _____ (Malikisi 1)
 - II. _____ (Malikisi 1)

- h. Pezani mawu Kuchokera m'nkhaniyo omwe ndi otsutsana m'matanthauzo ndi awa:
- I. Akunjata (Malikisi 1)
- II. Za nzeru (Malikisi 1)
- i. Kamwana kochedwa kaja kadaiwala chiyani? (Malikisi 1)
- j. N'chifukwa chiyani che Mphaka adagwidwa ndi mantha? (Malikisi 1)
- k. Perekani matanthauzo a zining'a zotsatirazi Kuchokera m'nkhaniyi
- i. Ndangodzithira tsabola m'maso (malikisi 1)
- ii. Samaonetsa chitsakano (Malikisi 1)
- l. N'chifukwa chiyani Melifa samayankha akayitanidwa ndi che Mphaka (malikisi 1)
- m. Perekani mutu wankhaniyi? (Malikisi 2)

GAWO C. (MALIKISI 10)

4. Werengani kankhanika ndipo muyankhe mafunso otsatirawo

Anthu nonse mwalandiridwa. Bota ndi ilo liri pamtengo wamangopo. Wofuna kupha ludzu akhoza kutero. Ntchito yathu tiyambira kumpanda kwa kachigundako poti ndiko kuli gang'a wambiri.

Mafunso

- a. Kodi ndi malonje anji omwe akuyankhulidwawa? (Malikisi 1)
- b. Malonjewa angayankhulidwe ndi ndani? (Malikisi 1)
- c. Angayankhule malonjewa ndani? (Malikisi 1)
- d. Kodi mawu oti kumpanda akutanthauzanji? (Malikisi 1)
- e. Kodi malipiro omwe amaperekedwa kwa sing'anga asanafune mankwala amatchedwa chiyani (Malikisi 1)

5. KUPANGA ZIGANIZO

- a. Sasa (Malikisi 1)
- b. Mtenthandevu (Malikisi 1)
- c. Womba (Malikisi 1)

d. Mosimbwa

(Malikisi 1)

e. Yedzeka

(Malikisi 1)

GAWO D (MALIKISI 40): Zungulizani lembo lokhoza (A, B, C kapena D) m' mafunso otsatirawa

Mafunso 6 mpaka 10: Sankhani mitundu yamawu omwe atsekedwa mzere kungsi kwawo

6. Mbewa idalowa kuuna.

- | | |
|-------------|--------------|
| A. Muonjezi | C. Mperekezi |
| B. Dzina | D. Mfotokozi |

7. Alinafe wabwera kasanu.

- | | |
|----------------|--------------|
| A. Mlowam'malo | C. Mfotokozi |
| B. Dzina | D. Muonjezi |

8. Ndidapita kwa aphunzitsi kukacheza.

- | | |
|----------------|--------------|
| A. Mlowam'malo | C. Mperekezi |
| B. Muonjezi | D. Mneni |

9. Koto! Ndachita tsoka.

- | | |
|------------|----------------|
| A. Mfuwu | C. Mlowam'malo |
| B. Mvekero | D. Mneni |

10. Anthu onse ali mnyumba mwanga

- | | |
|--------------|----------------|
| A. Mfotokozi | C. Mlowam'malo |
| B. Muonjezi | D. Mneni |

Mafunso 11 mpaka 15 : Sankhani matanthauzo a zining'a zotsatirazi

11. Kugunda mgolo

- | | |
|------------------|--------------|
| A. Kunama | C. Kuuluka |
| B. Kupeza palibe | D. kosochera |

12. Yabwidwa ndi chitedze

- | | |
|------------------|------------------|
| A. Lowa mtchire | C. Tenga matenda |
| B. Inva kuyambwa | D. Tenga mimba |

13. Wadya mfulumira

- | | |
|---------------|------------------|
| A. Wapupuluma | C. Wamwalira |
| B. Wachenjera | D. Walowa nyumba |

14. Mkukuluzi

- | | |
|------------------|----------------------|
| A. Njoka yolusa | C. Njala yoopsa |
| B. Mvula yoyamba | D. Chikuni chowawuka |

15. Waba mphasa

- | | |
|------------|--------------|
| A. Wadwala | C. Watopa |
| B. Wasauka | D. wamwalila |

Mafunso 16 mpaka 20: Sankhani chiganizo chomwe chili ndi zizindikiro za m' kalembedwe zoyenera.

16.

- | |
|---------------------------------|
| A. M'manja mudamveka kuti thya! |
| B. M'manja mudanveka kuti Thya. |
| C. M'manja mudanveka kuti thya. |
| D. m'manja mudanveka kuti thya. |

17.

- | |
|------------------|
| A. John, wanva. |
| B. John, wanva |
| C. John, wamva? |
| D. "John, wanva" |

18.

- | |
|----------------------------------|
| A. Zoti waponda njati, ndizoona. |
| B. Zoti waponda njati ndizoona. |
| C. Zoti waponda, njati ndizoona. |
| D. Zoti waponda njati ndizoona! |

19.

- | |
|--------------------------------|
| A. Ine simfiti, "iye adatero." |
| B. "Ine simfiti iye adatero," |
| C. Ine simfiti, iye adatero. |
| D. "ine simfiti," iye adatero. |

20.

- | |
|-------------------------------------|
| A. Ha! Zabwino adya ndi akanyimbi. |
| B. Haa: Zabwino adya ndi akanyimbi. |
| C. Haa, zabwino adya ndi akanyimbi. |
| D. Haa; Zabwino adya ndi akanyimbi. |

Mafunso 21 mpaka 25: Sankhani chachimuna kapena chachikazi cha mayina awa:

21. Nkhosa

- | | |
|-------------|------------------|
| A. Tonde | C. Thazi |
| B. Mphululu | D. Chipsolopsolo |

22. Atatavyala

- | | |
|--------------|-------------|
| A. Atsibweni | C. Amalume |
| B. Abambo | D. Apongozi |

23. Mfumukazi

- | | |
|--------------|--------------|
| A. Mperekazi | C. Wakunjira |
| B. Muphwa | D. Mfumu |

24. Mdzidzi

- A. Dona C. Chumba
B. Mfule D. Gojo

25. Ndoda

- A. Ntchembere C. Mnyamata
B. Malume D. Mtsikana

Mafunso 26 mpaka 30 : Sankhani magulu amayina omwe ali ndi mzere kungsi kwawo

26. Ukapolo udathetsa abale athu.

- A. I—Zi C. Mu—Mi
B. Li—Ma D. U—Ma

27. Nkhumba yawo yafa.

- A. Li—Ma C. I—Zi
B. Chi—Zi D. Ka—Ti

28. Ndatola kamba wathanzi.

- A. Ka—Ti C. U—Ma
B. Mu—A D. I—Zi

29. Iye walima mphepete mwa dambo.

- A. I—Zi C. ku—Pa—Mu
B. Li—Ma D. Mu—A

30. Kwawo kwagwa maliro.

- A. Li—Ma C. U—Ma
B. Chi—Zi D. Ka—Ti

Mafunso 31 mpaka 35 Sankhani ntchito za “ndi” m’ziganizo zotsatirazi

31. Wabwera ndi agogo ake.

- A. Mvekero C. Mperekezi
B. Mlumikizi D. Mlowam’ malo

32. Iye ndi waulesi

- A. Mneni C. Mlowam’ malo
B. Mperekezi D. Mfotokozi

33. Katunduyu ali ndi, kulemera.

- A. Mperekezi C. Mlumikizi
B. Mneni D. Mvekero

34. Nditenga chomwechi.

- A. Mneni C. Mperekezi
B. Mlowam’ malo D. Mvekero

35. Ndatenga mbatata, nthochi ndi mpunga.

- A. Mperekezi C. Mlumikizi
B. Mlowam’ malo D. Mneni

Mafunso 36 mpaka 40 : Sankhani mawu ofanana m’matanthauzo ndi awa

36. Machawi

- A. Mamawa C. Changu
B. Matowo D. Zovala

37. Chitsitsamsepe

- A. Mwana wachiwiri kubadwa
B. Mwana woyamba kubadwa
C. Mwana wofuntha
D. Mwana womaliza kubadwa

38. Mfisuro

- A. Chakudya cha usiku
B. Chakudya cham’ mawa
C. Chakudya chamazulo
D. Chakudya chodzidzira

39. Mayani

- A. Maloza C. Nyemba
B. Masamba D. Nthochi

40. Mbwanj

- A. Chinangwa C. Mbwanda
B. Nyemba D. Mbatata

Mafunso 41 mpaka 45 sankhani mitundu ya nthambi ya chiganizo yosaima payokha yomwe ili ndi mzere kungsi kwake.

41. Mwana amene akudwalayo si wanu.

- A. Ya dzina C. Ya mfotokozi
B. Ya muonjezi D. Yoima payokha

42. Poti mwabwera, ndidalitsa.

- A. Ya mfotokozi C. Ya dzina
B. Ya muonjezi D. Yoima payokha

43. Ndizoona kuti Ebola yavuta.

- A. Ya mfotokozi C. Ya muonjezi
B. Yoima payokha D. Ya dzina

44. Sankawerenga choncho walephera mayeso.

- A. Yoima payokha C. Ya dzina
B. Ya mfotokozi D. Ya muonjezi

45. Zomwe mwapatsidwazo ndizofunika kwambiri.

- A. Ya dzina C. Ya mfotokozi
B. Ya muonjezi D. yoima payokha

MAFUNSO ATHERA PANO !!!